

MUWAUZE KUTI NDIMAWAKONDA

Kulandira Cibvumbulutso Cha
Chikondi Cha Mulunga Pa Inu



JOYCE MEYER

#1 *NEW YORK TIMES* BESTSELLING AUTHOR

Unless otherwise indicated, all Scripture quotations are taken from
THE AMPLIFIED BIBLE: Old Testament.

Copyright © 1962, 1964 by Zondervan Publishing House
(used by permission); THE KING JAMES VERSION; and from

THE AMPLIFIED NEW TESTAMENT

Copyright © 1958 by the Lockman Foundation
(used by permission).

Copyright © 2014 by Joyce Meyer Ministries – South Africa

All rights reserved. No part of this publication may be reproduced, distributed, or transmitted in any form or by any means, or stored in a database or retrieval system, without the prior written permission of Joyce Meyer Ministries – South Africa.

Joyce Meyer Ministries – South Africa
PO Box 5, Cape Town, 8000

Phone: +27 (0) 21 701 1056
Website: www.joycemeyer.org

Go to tv.joycemeyer.org to watch Joyce's messages in a variety of languages

Tell Them I Love Them – Chewa
Not For Resale

ZA MKATI MWA BUKULI



<i>Poyamba Dziwani</i>	4
1. Mulungu Amakukondani	6
2. Kodi Ndine Oyenera?	12
3. Chikondi Ndi Ubale	20
4. Chikondi, Kukhulupirira Ndi Chikhulupiriro	26
5. Kumasulidwa Ku Mantha	32
6. Chikondi Chimafikira Konse	37
7. Chidzakusithani	44
Mukhale M'moyo Watsopano	49
Pemphero La Chipulumutso	51
Za Olemba Bukhuli	52

POYAMBA DZIWANI



Ndikukhulupirira kuti chomwe anthu akufunikira kwambiri kuposera china chiri chonse ndi bvumbulutso la chikondi Chake cha Mulungu kwa iwo eni ake. Ndikhulupirira izi zikhoza kukhala maziko a momwe chikhalidwe chopambanitsa cha m'mene Kristu ayenerera kuimila. Sitili ofunikira chidziwitso cha m'mutu mwathu cha chikondi Chake cha Mulungu; tiri kufunikira bvumbulutso. Ilo lingaperekedwe ndi Mzimu Oyera ndipo lingaperekedwe pamene okhulupirira aliyense alingalira za chikondi cha Mulungu, kuchionetsetsa chikondi cha Mulungu pa moyo wako ndiponso kufunafuna bvumbulutso limeneli kudzera m'Mau Olembedwa a Mulungu komanso kudzera mu pemphero.

Ndikosavuta ngakhale pang'ono kuvomereza kuti Mulungu amakonda dziko lonse ndithu ndi kutuma Yesu kudzafera dzikoli. Koma ndikuvutirako pang'ono kuti tikhulupirire kuti munakakhala munthu m'modzi yekhayo pa la dziko lapansi lino, kuti Mulungu amakukondani inu kwambiri zedi ndi kuti anakatha kutumiza Yesu kuti adzakufereni inuyo ndipo inu nokha basi.

Patapita zaka zambiri ndiri Kristu okhumudwa, ndinatha kumvetsa za chikondi Chake cha Mulungu. Mulungu mwa chisomo anandibvumbulutsira kwa ine, kudzera kwa Mzimu Oyera, chikondi Chake kwa ine mwini wake. Ili bvumbulutso limodzi limenelo linasithiratu moyo wanga onse ndi mayendedwe anga ndi Iye.

Ndikhulupirira kuti chimene inu mutawerenge mu buku ili chikubweretserani masomphenya atsopano ndi kumvetsetsa kokhudzana ndi za chikondi cha Mulungu. Ndikukhulupirira chikhazikitsa njala yatsopano mwa inu kuti mukakhale nalo bvumbulutso la inuyo nokha eni ake. Ndikukulimbikitsani kuti muwerenge bukhu mwa pang'ono-pang'ono, ndi kuligwiritsa ntchito ngati chida powerenga ndikuwalingalira za m'Mau a Bukhu Loyera ndiponso za zolingalira zimene inu mutazipeze mu matsamba otsatirana nawo omwe ali m'buku limeneli.

Bukhu ili laperekedwa kwa inu modzichepetsa zedi, pozindikira kuti ine sindiri kathu koserera Iyeyo ndipo bvumbulutsi la mtundu wina uli wonse ndi chidziwitso chomwe ndiri nacho cha m'Mau Ake, ndi chifukwa cha chisomo Chake basi.

1



MULUNGU AMAKUKONDANI

“Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi, kotero kuti anapereke mwana wake obadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo osatha.”

Yohane 3 ndime 16

Mulungu akufuna banja, ndiye Mulungu anatipanga ife kukhala ana Ake. Iye safuna kuti ife tidzichita ngati makanda ai, koma akufuna tidzikhala ngati ana Ake. Iye akufuna ife tidzidalira pa Iye, kukhazikika pa Iye, kutsamira pa Iye, kumukonda Iye ndi *kumusiya kuti Iye atikonde ife*. Iye akufuna ife kuti timukhulupirire ndi kufikira kwa Iye pamene tiri ndi chosowa. Iye akufuna kuti tikhale ndi ubale weni-weni waphuphu ndi *ife*.

Ambiri mwa ife timatenge Yohane 3 ndime 16 mu kumvetsera kwakukulube ndithu. “Ah, inde, ndikudziwa Yesu anafera dziko lonse,” koma ife *sitiri* ngati gulu la athu chabe pansu pano ai amene Yesu anawafera. Iye anafera wina aliyense wa ife. *Anafera Inu!*

Mukanakhala munthu *yekhayo* pa dziko lino lapansi, Iye anakangofera *inuyo* nokha basi. Anakanzunzika chimodzimodzinso chifukwa cha *inu* nokha basi. Anakuferani *inu!* Mulungu amakukondani inu kwambiri zedi. Amakukondani ndi chikondi

chopanda malire.

Tsiku lina ndinali kuyendetsa galimoto motsikira mseu wina, ndipo Mulungu anayankhula mu mtima wanga ndipo anati, Joyce, iwe ndi kamwana ka m'diso langa.” Ndipo sindinkadziwa kuti Mauwa ndi a mu Baibulo m'Bukhu Lopatulika, ai. M'dyerekezi anabwera ndi maganizo pambuyo pake peni-peni ndipo anati “Kodi kumeneko sikunyada kokha-kokha basi? Iwe ukudziganizira kukhala ndani kodi?” Ndiye ndinaganizira kwa ine mwini wake, “Ah sindikuyenera kumaganazira mwa mtundu otere ai.” Ndi zotsutsana ndi maganizo athu a umunthu kumadzizindikiritsa kuti *ndife* a mtengo wapatali, kuti ndife a mphatso yapadera, kuti ndife osiyana ndi wina aliyense. Wina aliyense wa ife ndi munthu pa iye mwini wake yekha, olengedwa ndi Atate Wathu kuti tikakhale osiyana ndi munthu amene ali pafupi ndi ifeyo.

Pamene ndinali nkuganiza za izi, Mulungu anandisonyezera ka chithunzi-thunzi kakang'ono ka munthu wa mayi ataima mu sitolo yogulitsa za kudya yaikulu pamalo pamene panali mulu waukulu wa zipatso za ma apozi (apples). Iye anayang'ana-yang'ana mofufufuza pamenepo ndipo napeza chipatso chimodzi chomwe chinali chachikulu kwambiri zedi ndipo analinatenga lomwe linali labwino zedi mwa onse pamenepo. Chimene Ambuye amandiuza pamenepo ndikuti ineyo ndi chipatso cha mtundu wa apozi (apples) chabwino kwambiri kwa Iye. Ine ndi wamtengo wapatali. Ichi sichiri ngati cholondola ai, koma mukhoza kuona kuti, Mulungu akuuza zimenezi kwa wina aliyense wa ife. Sikuti Iye akuti iwe ndiwe wina wake opanda banga, ndipo wina aliyense sikuti ndi wabwino ai. Iye akuti ife tiri a mtengo wapatali. Izi ziri mu Mau a Bukhu Lopatulika, ndipo Mau amenewa ndi a wina aliyense. *Ndiwe kamwana ka m'diso la Mulungu.*

Ine sindinalandire chimene Mulungu ananena kwa ine chifukwa ndinamva kukanizidwa poganizira za zinthu zokoma zotero za mwa ine. Patapita masiku awiri ndinatsegula Baibulo yanga pa Masalmo 17 ndime 8, ndipo apo ndinayanganizana ndi khope yanga: *“Ndisungeni monga kamwana ka m’diso, Ndifungatireni mu mthunzi wa mapiko anu.”* Ine ndinati, “Ooh, amene uja analidi Mulungu kani. Ine ndi kamwana ka m’diso la Mulungu.” Kwa nthawi yaitali kwambiri, ndinamva kukhala wa mtengo wapatali nthawi ina iri yonse yomwe ndinaganizira chimenechi.

Anthu ali ndi chilakolako, ndi kulakala, ndiponso chikhumbo mu mitima yawo yofuna kumakonedwa. Mulungu anatilenga ife kukhala a choncho. Anthu ambiri amakhulupirira kuti Mulungu amakonda dziko lapansi ndipo amamukonda Yesu, koma zimawavuta kukhulupirira kuti Mulungu amawakonda iwo. Koma Mau a m’Bukhu amatiphunzitsa kuti Mulungu amawakonda iwo chimodzi-modzi m’mene Iye amamukondera Yesu. Iye amakukondani chimodzi-modzi m’mene iye amamukondera Yesu. Tiyeni tione pa Yohane 5 ndime 20:

“Pakuti Atate akonda Mwana, namuonetsa zonse azichita yekha: ndipo adzamuonetsa ntchito zoposa izi, kuti mukazizwe.”

Apa Mulungu akuti, “Ine ndikupanga zinthu zazikulu izi kudzera mwa Yesu, ndipo zinthu zazikulu kwambiri zoposa izi kudzera mwa Yesu, kuti *inu* mukazizwe” (maganizo a wolemba bukhuli). Kodi mukudziwa kuti ndikotiyenera kuzizwa ndi chinthu china chake, kuti tikakhale mu zodabwitsa za zomwe Mulungu akuchita?

Timawerenga Mau a m’Bukhu Lopatulika amenewa, koma nthawi zambiri timasephana ndi zimene Mulungu akufuna kutichitira ife. Iye akufuna ife tikayangane zintchito zazikulu zimene Iye wachita kudzera mwa Yesu ndipo tikangizizwa ndi kunena kuti, “Abale,

Mulungu, izo ndizazikulu zimene munachita kudzera mwa Yesu.” Ndipo akufuna mukabvundukule mu Baibulo pa Yohane 14 ndime 12 pamene Yesu akuti,

“Wokhulupirira Ine, ntchito zimene ndichita Ine adzazichitanso iyeyu; ndipo adzachita zoposa izi; chifukwa ndipita kwa Atate.”

Mulungu adzachita zinthu zofanana kudzera mwa inu, ndi ntchito zazikulu zoposera izi mudzazichita chifukwa Yesu anapita kwa Atate wake. Kodi muli okhulupirira zimenezo. Kodi mukukhulupiriradi kuti kuti Mulungu amakukondani inu ndipo akugwiritsani inuyo nomwe ntchito?

Ambuye anatumikira kwa ine tsiku lina pamene ndinali mkuwerenga ndipo anati, “Joyce, Ine ndimawachitira anthu zinthu zambiri tsiku ndi tsiku chifukwa chakuti ndimawakonda, ndipo iwo izi samazona ngakhale pang’ono. Samazindikira zimenezi konse ai. Ine ndikupatse chitsanzo chimodzi chokha. Tsiku liri lonse Ine ndimayakhula kwa dzuwa ndimaliuzwa kuti ‘Muka,’ Ine ndinamupangira Joyce, Betty, Jamie, (apa ikanipo dzina lanu).”

Taimani ndipo ganizirani izi. Tsiku liri lonse dzuwa limatuluka mulengalenga kuwalira *inu*. Inde, dzuwa! Ndipo timangochitenga ichi mwa chizolowezi basi. Timangodziwiratu kuti dzuwa lituluka tsiku ndi tsiku, komatu limawalira *inuyo*. Pamene mvula imagwa munyengo yake, imagwera *inuyo*. Pamene kwagwa chisanu cha madzi ouma owundana, icho chimagwera *inuyo*. Mulungu amakukondani inu kwambiri zedi.

Pa Deutoronomo 7 ndime 9 ikuti,

“Chifukwa chache dziwani kuti Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu: chipangano ndi chifundo ndi iwo ndiye Mulungu

wokhulupirika, wakusunga chipangano ndi chifundo ndi iwo akumkonda ndi kusunga malamulo ache, kufikira mibadwo zikwi.”

Kodi inu mukuganizira kuti mibadwo zikwi ndiyotalika kokwanira kwa inuyo kuti mungathe kulowamo mu chikondi cha Mulungu? Mutha kuona, Iye ndi Mulungu wamuyaya, ndipo simungathe kumumalizitsa Mulungu ai. Ambiri mwa ife timaganizira kuti tamumalizitsa kumene Mulungu ndi zolephereka komanso zosokonezeka zathu, koma izi sizotheka konse. Chikondi sichingamalizitsike ai, ndipo simungathe kumupangitsa Mulungu kuti asakukondeni ai. Chikondi sichithu chimene Mulungu amachichita ai. Icho ndi Chimene Iye ali.

Ngakhaletu iye ochimwitsa moipiratu muja amene amayenda pathaka pa dziko lino amene angathe kulavulira m’maso mwa Yesu’yo ndikunena kuti, “Ndilibe nawe ntchito; ine ndiri wokwanitsidwa kwathuthu kupita ku gehena basi” Mulungu amamukonda ameneyo. Ndiye kungatheke bwanji kuti Iye asakawakonde iwo amene anasakhidwa ndikuwapatula ndi cholinga cha Mulungu?

Ndipo mwina inu mwanena kale kuti, “Ndinamulandira Yesu mumtima mwanga, ndipo ndimamukonda Iye.” Koma ndikufunsi inu, *kodi mumakhulupirira muyezo wanji Mulungu kuti amakukondani inu?*

Uwu ndi uthenga wophweka kwa inu: *Mulungu Amakukondani inu*. Koma awa ndi maziko ongoyambirira amenene Mulungu angathe kukhazikitsa mwa inu kuti inu mukathe kumvetsetsa china chiri chonse.

Kaya mwaphunzira chinthu china za Mulungu, ngati simungavomereze kuti chinthu chake cha mtundu wanji ndipo

mumawerenga kwambiri bwanji kusakatula zinthu za Mulungu, ngati simungavomereze choonadi chakuti Mulungu amakukondani, simungathe kupita nazo patali konse ai. Chikondi cha Mulungu kwa inuyo ndiye maziko a chikhulupiro chanu, cha ufulu wanu ku machimo ndiponso chothekera chanu kupita kukatumikira ena popanda mantha. *Kodi mulandira chikondi Chake kwa inu?*

Mulungu amamkukondani *inu!*

2



KODI NDINE OYENERA?

“Ndipo chiyembekezo sichichititsa manyazi, chifukwa chikondi cha Mulungu chinatsanulidwa m’mitima mwathu mwa Mzimu Woyera, amene wapatsidwa kwa ife.

Pakuti pamene tinali chikhalire ofooka (opandilatu mphamvu zozithandizira ife eni ake), pa nyengo yake Khristu anawafera (m’ malo mwawo) osapembedzera. Pakuti ndi chibvuto wina adzafera munthu adzafera wina olungama; pakuti kapena wina adzalimbika mtima kufera munthu wabwino.

Koma Mulungu atsimikiza kwa ife chikondi Chake cha Mwini Yekha (Chakechake) m’menemo, kuti pokhala ife chikhalire ochimwa, Khristu (Mesiah, wodzodzedwayo) anatifera ife.

Ndipo tsono popeza inayesedwa olungama (kukhululukidwa, kuyeretsedwa, ndikubweretsedwa mu ubale oyenerera ndi Mulungu) ndi mwazi wake, makamaka ndithu tidzapulumuka mkwiyo wa Mulungu mwa Iyeyo.

Pakuti ngati, pokhala ife adani ache, tinayanjanitsidwa ndi Mulungu mwa imfa ya Mwana wache, makamaka (kwenikweni) ndithu, popeza ife tayanjanitsidwa, tidzapulumuka (Kuombedwa kwa tsiku ndi tsiku kuchokera nkupsinjika kwa machimo) ndi moyo

wache (kuuka).

Aroma 5 ndime yake ya 5 mpaka 10

Ambiri mwa ife timakhulupirira kuti Mulungu amatikonda pokhapokha pamene sitinasokonezeke ndi china chake basi. Anthu ambiri sakondweretsedwa ndi iwo eni ake kwenikweni, ndiye iwo amaphera mphongo ndikuti Mulungu sakukondweretsedwa nawo. Komatu Baibulo likunena kuti, “*Munthu ndani kuti mumkumbukila?*” (Masalmo 8 ndime 4) Ife ndicholengedwa chake cha Mulungu basi, *ndipo Iye amatikonda ife chifukwa chakuti amatikonda.* Iye ndi chikondi. (1 Yohane 4 ndime 16).

Iye amakukondani, ndipo *ndinu a mtengo wapatali zedi.* Izi zikutathauza kuti ndinu opatulika zedi komanso a paderadera. Inu simukuyenera kukhala ngati ineyo ai, komanso ineyo sindikuyenera kukhala ngati inuyo ai. Ndipo tidzakhala okhumudwa pamene tidzayesera kukhala ngati wina aliyense. Chimene chimachitika ndi kungomupatsa mdyerekezi mpata kuti iye kuti sindife oyenera. Chomwe tikuyenera kudziwa ndi chakuti, ndi Mulungu, sitifunikira konse ai “kukhala oyenera.”

Kodi Yesu anakuferani inu chifukwa chakuti munali opambana ndi abwino, kapena Iye anakuferani inu chifukwa Iye anakukondani inu? Baibulo limati Iye ngati anakukondani ndithu ndi kukuferani inu, nanga ndi kothekera bwanji kodi, kukhulukiridwa ndi mwazi Wake, kodi tsopano amakukondani? (Aroma 5 ndime yake ya 8 ndime 9). Iye amakukondani zedi kothekera kumaphimba zolakwika zanu za tsiku ndi tsiku. Amakukondani zedi mothekera kukudutsitsani tsiku la lero mu mphamvu ndi kupambana.

Mulungu anandisonyezera chitsanzo tsiku lina cha m'mene Iye amaonera zolakwitsa ndinso zoperewera zathu. Tangolingalirani

kamwana kakang’ono, ka zaka zitatu kapena zinayi, amene amakhala ali kuonerera mayi wake ali kugwira ntchito zake za panyumba. Mwanayu amawakonda mayi ake kwambiri zedi kotero kuti amatenga kandowa kamadzi ndi kasanza kakang’ono ndi kupita pazenera la chithunzi pakhonde la kutsogolo kwa nyumba. Kamwanaka ndi kakazi kamagundika kupaka pazenera paja modzipereka ndithu kenaka natenga mapepala ofewa kumalizitsa kupukuta zeneralo.

Zoonadi, kuonetsetsa zimakhala zolemberera ndi zopakikapakika komanso ziri sopo yekhayekha. Ndipo mukaonetsetsa zimene mwanayo wachita, mudzazindikira kuti anagwiritsa ntchito sanza yanu ya pamtima, ndipo chomwe mungafune kuchita ndikungomupotokola khosi lake. Koma iyeyo amabwera kwa inu, ndi timau take tokoma ndikunena kuti, “Amayi, mayi, ine ndakutsukirani zenera, ndipo ndalitsuka bwino zedi. Ndimakukondani amayi.”

Mayi wa chikondi amanena kuti, “Ah, wandichitira ine chinthu chokoma zedi. Zikomo kwambiri pondithandiza ine.” Ndipo pamene mwana uja wakakhala wotanganidwa kwina ndi zina zake, mayiyo amakachotsa zimene zasokonekerazo ndipo kenako amakalimbikitsa kamtsikanako kuti asazachitenso zamtundu wotero.

Mulungu anandiuza kuti izi ndi zimene Iye amachita kwa ife. Iye nthawi zonse amachotsa zimene ife tasokoneza. Ngati tikuchita zabwino zimene ife timazidziwa kuzichita kwake, ndizo zimene Mulungu amafuna kuchoka kwa ifeyo kuti tizichite. Iye samayembekezera kuti tikachite chinthu chomwe ife sitingathe kuchichita ai. Iye angathe kutisitha ife ngati tiri ovomereza kunena kuti “Zoonadi Mulungu, ndipo ndalakwa. Ndayesetsa, ndipo

sindingathe kuzisitha zimenezi.” Tsopano Iye adzatha chifukwa Iye akudziwa kuti inu simungathe kukwaniritsa pa inu nokha kuposera ndi thandizo Lake.

“Pakuti Iye amene Mulungu anamutuma alakhula mau a Mulungu (amalalika uthenga Wake wa Mulungu Mwini Wake), pakuti Sapatsa mzimu ndi muyeso. Atate akonda Mwana, nampatsa (kuikiza, kulonjeza) zinthu zonse mudzanja lake.”

Yohane 3 ndime yake ya 34 ndi 35

Tsiku lina pamene ndinali kuwerenga, ndinali mkulingalira pa ndime ndipo ndinakuwa ndi chimwemwe pamene ndinazindikira kuti Mulungu samatipatsa ife Mzimu Wake ndi muyeso. Iye samatipatsa ife kam’nusu kakang’ono chabe ka ichi kapena kam’nusu kakang’ono chabe ka icho.

M’malo mwake, Iye amati, *“Eni, tengani chiri chonse chomwe Ine ndiri nachi.”* Muyezo uliwonse wa mphamvu ya Mulungu ndinso chikondi ulipo ndi wopezeka kuti uperekedwe kwa inu leroli. Iye ali ndi zonse zomwe mukuzifuna, ndipo Iye akufuna kuti inu muwulandire umenewu ndithu. Bwanji? Chifukwa Iye amakukondani inu. Simuyenera kukhala oyenerera kuti mukathe kukwaniritsa kuwulandira chifukwa chakuti simukanatha kuchita moyenerera kuti mukathe kukwaniritsa kuti mukaulandire munjira ina iri yonse. Simukufunikira kuti mukakhale owoneka moyenerera kapena ndi maonekedwe oyenerera. Mulungu akufuna apereke kwa inu chifukwa chakuti Iye amakukondani.

Pa Deutoronomo 7 ndime ya 6 ndi 7 AMP, Mulungu anati, *“Pakuti inu ndi mtundu wa anthu wopatulika wa Yehova Mulungu wanu; Yehova Mulungu wanu anakusa nkhani, mukhale mtundu wa pa*

wokha wa Iye Yekha, mwa mitundu yonse ya anthu akukhala pa nkhope ya dziko. Yehova sanakondwera nanu, ndi kukusankhani chifukwa chakuchuruka kwanu koposa mitundu yonse yina ya anthu, kapena kuchepera kwanu.”

Mulungu anasankha Aisiraeli kuti akakhale anthu Ache a mtengo wapatali, ndinso ngati mpingo Wache, ifeyo ndi Isiraeli woonadi weniweni wa lero. Ndiye mau a m’Baibulo amenewa ndi a inunso leroli chimodzimodzi m’mene analirinso kwa iwo. Iye anati, “Ine sindinakusakheni chifukwa munali fuko lalikulu padzikoli ai.” Titakhala ifeyo, zinganenedwe kuti, “Sindinakusakheni inu chifukwa chakuti munachita zonse moyenerera kapena chifukwa chakuti ndinu wokoma zedi.”

Iye akupitirira kunena kuti iwo anali ochepera chiwerengero kuposera wina aliyense. Kunena mwatcutchutchu, ngati inu muli ngati ineyo, mwina munali kuganizira kuti inu ndiye amene simuli oyenereratu kuposera wina aliyense pamene munali musanapulumsidwe. Koma pa ndime 8 AMP, Mulungu akuti,

“Koma Yehova anakuturutsani ndi dzanja la mphamvu, ndi kukuombolani m’nyumba ya akapolo, m’dzanja la Farao mfumu ya Aigupto, chifukwa chake Yehova akukondani, ndi chifukwa cha kusunga lumbiro lija analumbirira makolo anu.”

Apa ndipo pamalo pa mkuwe! Mulungu akuti, “*ndinakhazikitsa chikondi Changa pa iwe, ndipo ndinakuuza iwe kuti ndiwe oyera. Ndinakuuza ndiwe wa mtengo wapatali. Iwe ndinakusankha, osati chifukwa chakuti ndiwe wabwino ndi wokoma zedi, koma chifukwa chakuti Ine ndimakukondani inu.*” Kodi mumadziwa kuti Mulungu amafuna kuti inu muchite chiani tsiku la lero? Iye akufuna mubvomereze ndi kulandira chikondi Chake.

Ambiri mwa ife, vuto lathu lalikulu ndi lakuti sitimakhala okondweretsedwa ndi ife eni ake pa tokha. Sitimakhulupirira kuti Mulungu amatikonda, kapenanso ndi kuti wina aliyense amatikonda ife ndi komwe. Timaganizira kuti, *amenewa angathe bwanji – pamene ine ndiri muchisokonezo choterechi?* Ngati inu mumakhulupirira kuti ndinu oipa ndi onyansa, ndiye mukhoza kuganizira, kuoneka ndi kuchita ngati ndinu oipa ndi onyansa. Inu simungathe kuchirimika kuposera pa chinthunzi cha inu mwini chomwe muli nacho mkati mwa mtima mwanu.

Ine vuto langa lalikulu linali lakuti sindinali kukondweretsedwa ndi ine mwini wake, ndiye ndinkataya pafupi theka ndi theka lakenso ya nthawi yanga kuyesera kudzisitha. Ndinali kuganizira kuti ndimayakhula kwambiri zedi, ndiye ndinali kuyesera kumakhala chete. Komano ndikakhala chete choncho, ndimadzakhhalano okhumudwa, ndipo wina aliyense amafuna kudziwa chifukwa chiani ndinali chete. Ndiye kenaka ndimaganzira, *Koma munandiuza kuti pakamwa panga ndi papakulu ndine olongolola. Tandisiyani ine. Ndikungoyesera kukhala chete.*

Sindingathe kunena pano zaka zingati zinali kundichitikira zimenezi. Komabetu ndimakhala m'mavutobe ndi pakamwa panga. Anthu ambiri amene ali odziwa kuyankhula amakwatiwa ndi munthu amene ali ofatsa zedi. Ndiye zimangosonyezerano kwambiri kukula kwa pakamwa kwako, ndipo m'dyierekezi amakukumbutsa zimenezi pafupipafupi. Ndiyo ichi chimatchedwa kuti *chilango*.

Mulungu akufuna kuti inu mukakhale a ufulu mu chilango, koma zimatengera chikhulupiriro ndi kulimba mtima kuti mukakhale a ufulu. Kodi mukudziwa kuti mungakhale odziweruza mwa mtundu wanji sizingathe kulipira dipo la chinthu ndi chimodzi

chomwe cha cholakwika chomwe inu munachita? Choncho ndikovutiratu kuti mukakhulupirire kuti Mulungu amakukondani pamene mwachita cholakwa.

Nthawi yonse yathuthu M'dyerekezi amakhala akukukathamulani-kathamulani ndi malingaliro a m'mene mulili opanda pake, oipa ndi onyansa. “Wachitansotu pano,” iye amatero. “Iwe ukudziganzira kukhala ndani? Mulungu sangakudalitse ai, iwe chinthu chakuda chokalamba, iwe. Iwe sungathe kukachitira umboni wina aliyense panopo. Iwe sungathenso kuchita china chiri chonse chokhoza.”

Apa ndi pamene zimatengera kulimba mtima pochirimika kwa munthu wamkati mwako ndikunena kuti, “Atate, Ine ndalakwitsa, ndipo ndikukupemphani inu mwa mwazi wa Yesu kuti mundikhululukire. M'dyerekezi, uchokeretu. Yesu anapereka dipo la machimo anga, ndipo iwe ulibe gawo lako.” Ndiye, inu dzingopitani tsopano ndikumakasangalala, kasangalaleni. Koma mwina mungathe kumakaganizira, “Ndimangopitiriza kumachita-chitabe zauchitsiru zoterezi.” Ine ndinkaganizira zoterezinso, mpaka pamene ndinasiya kumaweruzidwa ndi zoterezi. *Pamene mwasiya kulangika pa izo zimene mwazichita, mudzaleka kuchita choncho.*

Kudziweruza ndi chilango ku makubwezeretsani m'mbuyo ndi kukukhumudwitsani mpaka pa muyezo okanika kukakhala wa ufulu. Zimatengera munthu olimba mtima kuti usakalangike. Mukuyenera inu kukhala olimba mtima mu chikhulupiriro ndi kuchilimika ndipo *kunena ai kwa kudziweruza*. M'dyerekezi amakuuzani inu kuti, “Ukutathauza kunena kuti iweyo sukhumudwa ndi zimenezo? Chifukwa, ukuyeneratu pang'ono pokha kukhumudwa nazo zimenezo kwa maola ochepa okha. Chimene chija unachita iwe chija sichinthu chabwino.” Inu,

basi mudzingoti, “Ai, sindiri ndi chikhulupiriro chimenecho. Inetu sindikhumudwa konse ndi zimenezo.” Nyengo zingapo zoyambirira zidzakhala zovuta, koma zimakangotengera katatu kapena kanayi, ndipo mudzapachika zimenezo.

Pa Yesaya 53, ndime ya 5,6 ndi 11 mu *Baibulo la (Amplified)* likutiya ife za m'mene Yesu anatengera kwathuthu machimo athu ndi kuti iyenso anasenza kuweruzidwa (kuphatikiza chilango). M'dyerekezi safuna kuti inu mukhale a ufulu ku chilango china chiri chonse ai. Chifukwa kodi? Chifukwa inu mukalandidwa, simukaothera kwenikweni mu chikondi cha Mulungu. Chilango chimakusiyansani inu ndi Mulungu ndipo chimabwera pakati pa inu ndi Mulungu ngati chipupa cha chitsulo. Inu simungathe kumamuona Atate pamene mwaima m'chiweruzo. Chimene inu mumaona ndi chiweruzo ndi machimo patsogolo panu basi.

Yendani mu ufulu womasulidwa ku chilango ndipo khulupirani kuti pamene Mulungu anati chisomo Chake ndi chokwanira kuphimba ngakhale machimo anu, Iye anali kutathauza zoonadi. Iye amakukondani, ndipo chisomo Chake ndi kukhululuka ndi mphatso za ulere. Zilandireni lero!

Mulungu amakukondani *inu!*

3



CHIKONDI NDI UBALE

“Ndipo ife tazindikira (tamvetsa, tadziwa, tiri a tcheru ndi kuonetsetsa ndinso kudutsamo) ndipo takhulupirira (Kugwirizitsa ndi kuikapo chikhulupiro ndi kudalira) chikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m’chikondi akhala mwa Mulungu ndipo Mulungu akhala mwa iye.”

1 Yohane 4 ndime 16 AMP

Kodi tingatheke bwanji kukhala a tcheru ndi kuzindikira chikondi cha Mulungu? Ngakhale Iye atakukondani mwa mtundu wanji, ngati simuli a tcheru ndi kuchizindikira icho, sichingakuchitireni inu ubwino. Mukudziwa m’mene zimakhallira wina wake akamakusonyezzerani inu chikondi chambiri? Inu mumamva kutethera kokoma mkati mwanu kotero kuti dzikoli mumangoligwira mtchira basi chifukwa chakuti wina wake amakukondani inu. Mulungu amakukondani inu, ndipo Iye akufuna kukusonyezani chikondi chimenecho. Akufuna kuti inu mudzikhala ndi nthawi pamodzi naye tsiku ndi tsiku.

Kodi inu muli ndi ubale weniweni wa inu mwini ndi Mulungu? Kungoti chifukwa chakuti inu munapulumsidwa kale kale ndithu sikutathauza kuti inuyo muli mu m’chiyanjano cholemererapo ndi

Mulungu ai. Pamene ndimatsegula maso anga m'mawa, chithu choyamba chimene ine ndimaganizira ndi za Mulungu, ndipo Iye ndi chinthunso chomalizira chimene ndimaganizira ndisanakagone usiku. Ndipo ndimamuthokoza Mulungu mkatimkati mwa tsiku liri lonse. Palibenso chinthu china chiri chonse chimene ine ndimachifuna pa dziko lino lonse lapansi kuposera kumutumikira Mulungu ndi kumukondweretsa Iye. Ndipo ichi ndi choyenera china chiri chonse chimene inu mungatule pansu kuti mukachipeze chimenechi.

Mkati mwathu muli malo obooledwa amene ali ndi chibowoo chokhalapo mulungu amene ndi Mulungu Yekha amene angathekere kukakhazikikapo mowatseka pamenepo. Palibe icho chimene inu mungathamangirepo kapena mungachikhumbe chimene chingathe kutsekeketsa malo amenewa. Inu mukhoza kunena kwa inu nokha, "Izi ndikuzidziwa kale ine, ndinamulandira kale Yesu." Koma inu kodi mukumulandira Iye pa mphindi iri yonse, tsiku ndi tsiku, muzochitika zina ziri zonse? Kodi mukulandira chikondi cha Mulungu?

Mulungu amakukukondani Inu, ndipo ndinu a mtengo wapatali kwa Iye. Iye anatilenga ife kuti tikayanjane naye Iye. Ichi ndiye chokhumba chake cha Iye chopambanitsitsa ndinso chifuniro chake chenichenicho pa miyoyo yanu. Iye amatsamira pa guwalo m'mawa uliwonse ndi kumanena kuti, "Moni m'mawa wabwino, Ine ndimakukonda iwe."

Mzanga wina anali ndi maso mphenya ali kupemphera. Anawaona Atate akupita mu makomo a anthu akuno ku Amerika atadzuka m'mawa. Iye amapitamo ali okonzekera kukayanjana nawo ndi ku kayankhula nawo iwo. Iye amatenga mpando Wake wa pagome ndi kukhala pansu. Anthuwo' amaiimirira, ndikubwera,

ndikupita, ndikubwera, ndikupita. Iwo amamuuzabe Mulungu, “Nthawi ina. Khalanibe pomwepo kwa kanthawi pang’ono, Inu Mulungu. Pamene ine nditangomalizitsa izizi, ine ndiyakhula ndi Inu. Ine ndiyanjana ndi Inu posachedwetsapa, Inu Mulungu. Posachedwapa, Inu Mulungu. Posachedwapa, Inu Mulungu.”

Pakafika pa mapeto pa tsiku, ndiye mtsikana amene anawona izi ananena kuti mtima wake unasweka chifukwa anawona Mulungu, ndi mapewa akugwa, akutuluka pakhomo pamenepo. Ndipo panalibe aliyense amene anapita kukamuyakhula Iye tsiku limenelo.

Inu musatanganidwe. Ngati mulibe nthawi yopemphera ndi kukhala ndi Mulungu, ndiye kuti ndinu otanganidwa kwambiri. Pezani nthawi kumuuzza Mulungu kuti inu mumamukonda kwambiri bwanji. Pamene china chiri chonse chidzadutsa ndipo zonse zatha koma mkuwe, sipadzakhala china chiri chonse koma Mulungu. Ndi zimenezotu. Ndipo ngati inu mulibe ubale ndi Iye ndiye, padzakhala pocheredwerapo kuti muyambepo kufika pa ndime imeneyo. Sizikutathauza kuti inu simudzapita kumwamba ai, koma mwasemphana ndi chimwemwe chokhala moyo wopambana.

Ine ndiri kukumemani kuti mungochipatula chaka chathuthu, *ndi kumusiya Mulungu kuti adzikukondani inu.* Siyani kuyesera kuchita ndi mphamvu zanu ndipo kuchita ndi chikhulupiriro ndi kukhala m’mayi kapena m’bambo wa Mulungu wachikhulupiriro komanso wamphamvu. Tangodzibwezani ndi kuchita ngati kamwana kakang’ono. Inu mumangokwawira pa miyendo pa Atate wanu, ndipo kumusiya kuti Mulungu akukondeni inu. Inu simungathe kuti mumukondenso Iyeyo pamene simunathe kumulola kuti akukondeni inuyo kaye.

Yohane Oyamba 4 ndime 16 AMP amati,

“Ndipo ife tazindikira (tamvetsa, tadziwa, tiri a tcheru ndi, poonetsetsa ndinso kudutsamo) ndipo takhulupirira (Kugwirizitsa ndi kuikapo chikhulupiriro ndi kudalira) chikondicho Mulungu ali nacho pa ife...”

Kodi inu munadzuka m’mawa walero ndi kukhala nayo nthawi kuganizira za chikondi cha mtundu wanji chomwe Mulungu amakukondani inu? Pamene mwangodzuka m’mawa, simukonda kawirikawiri kupanga kalikonse. Koma mumafunikira kugwiritsa ntchito kamwa lanu kuti mukalitsitsimutse thupi lanu ndi kulola mzimu wa umunthu ukamuke ndi kukachita zinthu za mtundu wina uliwonse zokoma.

Ndiye pamene inu mwadzuka m’mawa, mukuyenera kuyamba kunena kuti, “Ah, Atate, ine ndiri kukuthokozani kuti Inu mumandikonda ine kwambiri zedi. Ndiri kukuthokozani kuti Munatuma mwa Wanu Yesu kudzandifera ine. Ah, Atate, ndikukuthokozani kuti ndiri ndi Mzimu Woyera. Ndiri kukuthokozani kuti mphamvu ya kuukanso iri mkatikati mwa ine. Ah, Ambuye, ndiri kukuthokozani kuti kuli konse kumene ine nditapite lero ndikakhala m’dalitso. *Mulungu, Inu mumandikonda ine. Inu mumandikonda ine*, mom’muno mu nyumba yanga ya ing’ono ino. *Inu mumandikonda ine!* Ine ndine mwana Wanu wanu wa mtengo wa patali. Ndine kamwana ka m’diso lanu. Inu mumandikonda ine!”

Mukumayenera kumadziyakhula inu mwini ndi kudzipatsa *tcheru* ndi *kuchilimika* kuti mwazengeleze komanso kumizidwa mu chikondi cha Mulungu. Baibulo limati Mulungu anali nacho chithunzi chako cholembedwa pa chikhatho cha manja ake. (Yesaya 49 ndime 16 AMP) Ine ndikutha kumuona Iye

m'mwambamo akunena kuti, tayang'ana, waona zimenezi? "Ah, siwokongongola iyeyu? Ine ndimangomukonda iyeyu kwambiri. Tangowayang'anani ana Anga, m'menemomo mu chikhatho cha manja Anga." Iye ali nanu *inu* m'menemo ngati choma mukumbutsira kumbutsira Iye kuti amakukondani ndipo amalalakala kumayanjana yanjana ndi inu.

Kumbukirani kumathokoza-thokoza pa Mulungu ndikumanga naye ubale wa chiyanjano. Nthawi zina mumafunikira kudzigwetsera pansi pa khope yanu mupemphero ndi kungomuthokoza Mulungu kuti ndinu opulumutsidwa. Tangobwererani ndi kumukonda Mulungu. Tawerangani pa 1 Yohane 4 ndime ya 16 ndi 17 AMP pamene Iye akuti,

"...Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m'chikondi akhala mwa Mulungu ndipo Mulungu akhala mwa iye."

M'menemo (umvano ndi chiyanjano ndi Iye) chikondi chathu chikhala changwiro kuti tikhale nako kulimbika mtima m'nsiku la milandu.."

Kudziwa kuti Mulungu amakukondani kumakulimbisani inu mtima mwa Iye ndi kukhulupirira kukhulupirika Kwake.

Madalitso onse adzabwera mukalola kuti Mulungu akukondeni Inu: chikhulupiriro chachikuludi, kuwapambana machimo, kuchilitsidwa, kuchita bwino ndi chimwemwe. Izi zikuyenereka kubwera pomulola Mulungu kuti akukondeni. Nthawi zambiri timatembenukira uku ndikuganizira, "Chabwino, ndiri kuyenera kumukonda Mulungu." Ine ndikukhulupirira tikuyenera poyamba kusiya Mulungu atikonde ife kaye. Sindikukhulupirira kuti mungathe kusonyezera chikondi chanu kwa Mulungu mpakana inuyo mutamulola Mulungu kuti akukondeni inu.

Inu ndikukuuzani kuti muyanjane ndi Mulungu ndipo mukufunikiradi kuyanjana ndi Mulungu, koma mungachite izi bwanji? Pamene Mulungu anandiiza ine kuti ndiyanjane naye Iye, ine ndinangopita pa mpando wanga waukuru ndikukakhala pansa ndi kunena kuti, “Tsopano chiani pano, Mulungu?” Indedi ndi choncho! Ine sindinkadziwa kuyanjana ndi Mulungu chifukwa, pa nyengo imeneyo, sindinali kudziwa kwenikweni kuti Mulungu amandikonda kwambiri bwanji.

Kodi inu mumasonyeza bwanji anthu m’mene mukumvera zinthu, ndithudi tangowakondani ndi kuwapatsa ulemu, ngati mulibe chikhulupiriro kuti iwo amakukondani? Inu mukhoza kumaopa kuti mwina mudzipusitsa inu nokha. Mumakhala omasuka ndi iwo okhawa amene mukudziwa kuti angathe kukukondani ndikukulandirani inuyo. Ine ndimakhoza kunena zinthu ndi mwamuna wanga zimene sindingathekere kunena ndi wina aliyense chifukwa chakuti ndimadziwa kuti iye amandikonda ine. Ndi chimodzimodzinsu ndi Mulungu. Ndiye tatulukani kunja ndi kuyambapo. Tampatsani Mulungu mpata, ndipo Iye akuphunzitsani m’mene mungathere kuyanjana Naye. Tadzifunsani nokha funso ili panopo: *Kodi ndine omasuka ndi Mulungu?*

Mulungu amakukondani *inu!*

4



CHIKONDI, KUKHULUPIRIRA NDI CHIKHULUPIIRO

“Pakuti mwa Khristu Yesu kapena mdulidwe kapena kasadulidwe kulibe mphamvu; komatu chikhulupiriro chakuchititsa mwa chikondi.”

Agalatiya 5 ndime 6

Ambiri mwa ife timataya nthawi kumayesera kukhala ndi chikhulupiriro. Tikudziwa kuti popanda chikhulupiriro sitingathe kumukondweretsa Mulungu (Ahebri 11 ndime 6), ndiye timagwira ntchito ndikumayesetsa kukhala nacho chikhulupiriro chambiri. Koma chikhulupiriro ndi cha m’mitima, ndipo umakachipeza kudzera mu ubale wa m’chijanano chokondana ndi Mulungu basi. Ine sindingathe kukuphuzitsani inu chikhulupiriro, ai, koma ndingakuphunzitseni zofunikira zake zokha za chikhulupiriro ndi kukupangitsani kukhala ndi chinjala cha ichochi ndipo mudzachita chiri chonse chothekera kuti muchipeze. Icho chimabwera ndi bvumbulutso la kwa Mulungu basi.

Siyani kuyesetsa kwambiri zedi kuchipeza chikhulupiriro ndi kumukondweretsa Mulungu, ndikuyamba kukhala ndi nthawi ndi kuyesera kwa Mulungu, kumukonda Iye. Tamangozungulirani

tsiku lonse kumukonda Iye ndi kumulola Iye kuti akukondeni.

“Pakuti tiyenda-yenda mwa chikhulupiriro (timaunyereza moyo wathu ndi kumazipangitsa ife eni ndi kudzitsimikizira kwa ife eni kapena chikhulupiriro cholemekeza ubale wa munthu ndi Mulungu ndiponso zinthu zopatulika, mokhulupirika ndi kukonderedwa koyera; timayenda m’menemo) si mwa maonekedwe.”

2 Akorinto 5 ndime 7 (Amp)

Nthawi ina pamene ndinali kuwerenga mau a m’Bukhu Lopatulika, Mulungu anayamba kundiyankhula zinthu zina za padera mu mtima mwanga. Ine ndikuyesera kuyenda mu chikhulupiriro. Mu chinthu china chiri chonse cha m’ moyo wanga, ndikufuna kuyenda mu chikhulupiriro. Ndipo Baibulo la (Amplified) likunena pa 2 Akorinto 5 ndime 7 kuti,

“...timaunyereza moyo wathu ndi kumazipangitsa ife eni ndi kudzitsimikizira kwa ife eni kapena chikhulupiriro cholemekeza ubale wa munthu ndi Mulungu.”

Tikhoza kungotinsu mu mau ena, *ine nditha kuyenda mu chikhulupiriro pokhazikika pa chimene ine ndimakhulupirira mu ubale wanga ndi Mulungu.* Kodi mukumvetsa pamenepa? Munthu amene amakhulupirira kuti ndi osalungama amatha kuiwalira kuyenda mu chikhulupiriro. Munthu amene amakhulupirira kuti ndi nyongolotsi yakale ya mufumbi ndipo Mulungu samamukonda iye akhoza kungoiwalirapo za kuyenda mu chikhulupiriro, nayenso. Anthu ambiri akuyesetsa kuyenda mu chikhulupiriro, koma alibe zinthu zina izi mu mitima yawo.

Agalatiya 5 ndime 6 ikuti, chikhulupiriro chimachititsa chikondi. Mulungu anachiika ichi mu mtima mwanga: “Aliyense amaganizira

kuti mau a m'Bukhu Lopatulika amatathauza kuti ngati sakonda anthu ena, chikhulupiro chawo sichigwira ntchito. Sizimene zimatathauza pamenepa ai. Chimene chimatathauza ndi chakuti iwo sadziwa kuti Ine ndimawakonda bwanji, chikhulupiro chawo sichigwira ntchito.” Chikhulupiro sichigwira ntchito popanda chikondi. Koma sikuthekera kwanu kukonda anthu ena, ai. Ndi kungomulora Mulungu amene ali Wamkulu kukondani inu.

Pali kusiyana kwakukulu pamenepo. Kumukhulupirira Mulungu ndi kuyenda mu chikhulupiro ndi kutsamira pa Iye pa china chiri chonse. Inu simungathe kuchita ichi ndi wina wake ngati musakudziwa kuti iye amakukondani. Mukhozanso kungoiwalapo basi. Simungathe kumudalira Mulungu ngati musakudziwa kuti Iye amakukondani inu.

Munakakhala mumadziwadi kuti Mulungu amakukondani bwanji inu, munakakhala ndi vuto pang'ono kulandira machiritso. Inu munakakhala ndi vuto pang'ono kukwaniritsa kulandira zosowekera za chuma chanu.

Chifukwa chomwe inu simungathe kulandiladi ndi chakuti inu simukhulupiriradi, kwathuthu, kuti Mulungu akukupatsani inuyo. Mukhoza kunena kuti, “Ine ndikufuna kukhulupirira zimenezo, koma ndikhulupirira bwanji?”

Muli ndi chikondi cha Mulungu mkati mwanu, ndipo zonse zomwe mukufunikira ndi kungoyamba kukachizindikira Iyeyo akamachisonyezera kwa inu. Baibulo likuti, “*tikonda Iye, chifukwa Iye anayamba kutikonda*” (1 Yohane 4 ndime 19). Kunakakhala kosatheka kuti ife tikamukonde Mulungu ngati sitinatstimikiziridwe za choonadi chakuti Iye anatikonda ife poyamba.

Ziri zonse pansi pa mkati mwa inu, m'mitima yanu. Ziri

m'menemo! *Mulungu amakukondani inu! Ndinu wokoma! Ndinu wokongola! Ndinu wokondeka! Ndinu opambana! Mulungu amakukondani inu!* Palibe wina aliyense mu dziko lino amene angathe kukukondani inu ngati m'mene Mulungu amakukonderani inu.

Inu *simufunikira* winanso aliyense koma Mulungu, koma iye adzakupatsani anthu ena m'moyo mwanu. Choonadi chake ndi chakuti pakanakhala popandanso wina aliyense koma inu nokha ndi Mulungu, zinakatha kumangokuyenderanibe bwino. Mulungu adzakhala bwenzi lanu leni-leni. Iye angakhale amene mungathe kukhala naye ngati inu mulibe. Iye angakhale Mayi wanu ndi Bambo wanu ngati inu mulibe.

Mulungu amakukondani inu kwambiri. Ndi m'mene inu mungakhulupirire Iye china chiri chonse. Iye amakukondani kwambiri kotero kuti amafuna kuti inu mukhale nacho. Ndipo mpakana mutazindikira kuti Mulungu akufuna kuti inu mukhale nacho, inu simudzapezeka mukugwira ntchito mu chikhulupiro chokwanira kuti mulandire china chiri chonse.

Chikhulupiro chimagwira ntchito pomulola Mulungu kuti akukondeni inu. Sichigwira ntchito chifukwa cha kuthekera kwanu kupita kwina kwake uko ndi kukamukonda wina wake kumeneko. Tamulorani Mulungu akukondeni ndi kukatha kukazungulira kwinku mukukamuza Mulungu, “Ah, Mulungu ndikudziwa ine mumandikonda ine. Alleluya! Atate, ndikukukwezani Inu. Ndikukuza dzina Lanu.”

Bambo Smith Wigglesworth anali Mtumiki wa Mulungu. Wina wache anamufunsa iye ngati anali ndi nyengo zazitali zitali zomapemphera, ndipo iye anati, “Ndikamodzi kamodzi kamene ine ndimapemphera kopoera mphindi zokwanira makumi atatu (30),

koma ndikamodzika modzinso pamene ndimadutsitsa mphindi makumi atatu (30) ndisanapemphere.” Iye anati mwanthawi ya kamodzi pamene iye amadutsa mphindi zoposera khumi limodzi ndi mphambu zisanu (15) nthawi ina osalumikizana ndi Mulungu, iye amayenera kulapa.

Ife timayesera kutenga zinthu kuchoka kolakwika. Simungathe kuzichita kuti zitheke zimenezi ndi ntchito zanu. Mulungu adzakudalitsani inu chifukwa chakuti Iye amakukondani inu. Iye adzakupatsani inu mu njira yomweyo imene Iye anakupatsirani chipulumutso.

Inu simungathe kutenga m’modzi wa m’banja lanu, kapena wina wake, kupulumutsidwa pogwira ntchito pa icho, ai. Kaloleni kuti Mulungu akukondeni, Kenako, pa nthawi imene mukuwonana ndi m’modzi wa m’banja lanuli, mudzakhala okonzeka kumukonda. Baibulo likuti ngati muwakonda iwo ndi kusiya kuyesera kuwakopa iwo ndi mau anu ndi njira zanu zonse zoziyenereza, mudzatha kuwakoka iwo kwa Yesu. Mzimu wa Ambuye udzatha kukoka banja lanu kudzera mu chikondi Chake. Koma simungathe kuwakonda ena pamene simunathe kumukonda Mulungu poyamba.

Aefeso 2 ndime 8 AMP ikuti, *“Pakuti muli opulumutsidwa ndi chisomo (kukondera kwa Mulungu kopanda zoyenereza) chakuchita mwa chikhulupiro...”* Kodi mukudziwa kuti simunanapange chiri chonse kuti mupulumutsidwe? Ambiri mwa ife pamene Yesu anatipulumutsa tinali ovundiratu ngati m’mene limatalikira tsiku, ndipo zachidziwikire kuti sizinatengere ntchito zanthu zabwino kapena kuthekera kwathu kuchita china chiri chonse. Chinali chifukwa cha chinthu chimodzi chokha: Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapereka Mwana

Wake obadwa yekha kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike koma akhale nawo moyo osatha. (Yohane 3 ndime 16).

Chisomo chikhozanso kukhala kuti kuvomereza kwa Mulungu kugwiritsa ntchito kuthekera kwake m'moyo mwathu kukwaniritsa zosowa zathu. Chimodzimodzi m'mene Mulungu, ndi chisomo, anakupatsani chikhulupiriro chokwanira kuti mukapululumutsidwe, Iyenso, chifukwa cha chikondi chake, anakupatsani chikhulupiriro kuti mukakhulupirire Iye ndi m'chiritsi. Amakupatsani chikhulupiriro kuti mukakhulupirire kuti Iye ndiye wopatsa.

Ngati chikhulupiriro chimene anatsanula cha chipulumutso chanu chinali chokwanira kukupulumutsani ku machimo anu onse, chikhulupiriro chomwecho chiri mkati mwanu momwemo chotheka kukwaniritsa zosowa zanu zonse pa moyo wanu wonse. Ngati mukukhulupirira kuti Mulungu amakukondani inu, ndi kuyamba kuzindikiradi, ndiye mutha kuyambadi kumudalira Iye. Mudzatsimikiziridwa za choonadi chenicheni cha Mau a Mulungu. Mudzazindikira kuti sadzakunamizani inu konse, ai chifukwa Iye amakukondani inu. Monga mu Baibulo ya (Amplified), “chikhulupiriro” ndi “ndi chiphunzitso cha umuthu wanu onse wa inu yeni pa Iye” (Mulungu) “ndi kudalira kwenikweni ndi kulimba mtima mu mphamvu Yake, nzeru, ndinso ubwino” (Akolose 1 ndime 4). Pamene mulola kuti Mulungu akukondani inu, ndipo mudzakhala nacho chikhulupiriro.

Mulungu amakukondani *inu!*

5



KUMASULIDWA KU MANTHA

“Mulibe mantha mu m’chikondi; (kuopa sikupezekapo ai), koma chikondi changwiro (chaphuphu, changwiro) chitaya kunja mantha, popeza mantha ali nacho chilango, ndipo (ndiye) wamanthayo sakhala wangwiro m’chikondi (iye sanakulitsitse kwenikweni mu chikondi chathuthu changwiro).”

1 Yohane 4 ndime 18

Nthawi zambiri zimatiyendera bwino kwambiri mu chikhulupiriro, kulimba mtima kuti Mulungu amatikonda ife, kumudalira. Koma mwadzidzidzi, china chake chimatichitika pa ife.

Wakuba wamkulu wa chikhulupiriro ndi zotichitikira - zinthu zoipa zimene zimatichitika kwa ife. Inu mulibe vuto lalikulu konse kukhulupirira kuti Mulungu amakukondani inu mpakana zitakuchitikirani zokuchititsani kuona ngati Iye samakukondani, ai.

Ndiye tsopano m’dyerekezi amafika ndi mantha ndi chilango kuti akakusiyanseni inu ndi chinthu chenicheni chomwe chingakumasuleni inu - chikondi cha Mulungu, “Chabwino, nanga izizi bwanji?”

Iye amatero. “Kodi ndimayesa Mulungu amakukondani inu.

Nanga ndi chifukwa chiani zinthu zoipa chonchi zikukuchitikira ivelyo? Ndiye kuti unachita china chake choopsya zedi. Mulungu wakukwiwira iwe zedi.”

Ndiye kulimbika mtima kwako kumasowa pamaso pa Mulungu, ndipo Iye sangathe kuku thandizati iwe ngati siuli olimba mtima, ai. Iwe sungathe kulimba mtima, kapena kudzala ndi chikhulupiriro, ngati sukudziwa kuti Mulungu amakukonda. Ndipo iwe ukalandira mtolo wa m’dyerekezi wa mantha ndi chilango, sumadziwa m’mene Mulungu amakukondera iwe.

Yohane Oyamba 4 ndime 18 ikunena za chinthu cha mphamvu koposa kwambiri “...*chikondi changwiro chitaya kunjira mantha.*” Ine ndimalingalira ndi kulingaliranso pa mau amenewa a m’Bukhu Lopatulika, kuyesera kumvetsetsa chimenechi, ndipo tsiku lina kumapeto kwake Mulungu anandigwetsera mu Mzimu wanga. Chikondi changwiro chimataya mantha, ndipo Mulungu ndiye chikondi changwiro. Ndipo pamene mumadziwa m’mene chikondi changwiro chimenechi chiliri kwa inu, palibe china chiri chonse mu chilengedwe chomwe mudzachita nazo mantha inu. Ndikosatheka kuti inu mukachite mantha ngati muli ndi bvumbulutso la inu eni kuti Mulungu amakukondani inu.

Ndikosatheka kuti inu mukachite mantha olephera ngati mukudziwa kuti Mulungu amakukondani inu. Inu simungalephere ai, ngati muli odalira pa Mulungu. Mungathe kulephera pokhapokha pamene inu muli kudalira mwa inu nokha. Ngati mumadziwa kuti Mulungu amakukondani inu, simudzaopa kukanidwa.

Chikondi cha Mulungu ndi cha mulingo wotero ndithu chimaphimba china chiri chonse. Kodi mukuganiza kuti Mulungu

yemweyo amene anakupulumutsani inu ndi kukumasulani inu angathe kukulangani inu? Satana ndiye amene amalanga. Mulungu akakutsimikizira inu za tchimo la m'moyo wanu, ndipo Iye adza kusonyezerani inu njira imene inu mungatulukire. M'dyerekezi amakulangani inu ndipo kumakuuzani inu kuti palibe njira yotulukira.

Mu Baibulo la (Amplified) mau a m'Bukhu lopatulika akuti:

“Mulibe mantha mu m'chikondi; (kuopa sikupezekapo ai), koma chikondi changwiro (chaphuphu, changwiro) chitaya kunja mantha, popeza mantha ali nacho chilango, ndipo (ndiye) wamanthayo sakhala wangwiro m'chikondi (iye sanakulitsitse kwenikweni mu chikondi chathuthu changwiro).”

1 Yohane 4 ndime 18

Anthu ambiri amaganizira kuti mau a m'Bukhu Lopatulika amatathauza kuti ngati inu ngati mungandikonde ine kokwanira, ndiye kuti simungathe kumandiopa ai, kapena mukamukonda wina wake kokwana, ndiye kuti mantha adzachoka m'moyo mwanu. Koma sizimene zimatathuzatu zimenezo ai.

Zimatathauza kuti ngati mutalole Mulungu kukukondani inu, ndiye kuti simudzakhala amantha. Mukuyenera kumulola Mulungu kuti akukondeni inu ngati musakufuna kukhala a mantha m'moyo wanu. *Landirani chikondi cha Mulungu kwa inu pompanopa ndi chozizwa cha chikhulupiro.* Fikirani mu chikhulupiro ndipo tengani chikondi cha Mulungu kwa inu.

Pamene Mulungu anali atangondipatsa ine bvumbulutso limeneli la chikondi Chake kutaya mantha, ndinayamba kuchichita ichi. Tinali ndi vuto ndi galimoto lathu, ndipo tinali nkuganizira kuti

mayendedwe a injini, ndipo injiniyo inali yaikulu ndithu! Mwina zinakakwanira pafupifupi mazana a ma kwacha anayi kapena asanu (forty or fifty) kwacha kuti tigulire injini ina ngati iyo inali yoti ndi yonongekeratu, ndipo pa nthawiyo tinalibe ndarama. Choncho tinangopitirizabe kumaiyenderabe.

Mulungu ananditumikira ine m'mawa umenewo ndipo anati, "Mai Joyce tamangoyenda kumazungulira-zungulira ukundikonda Ine, ndipo undilore Ine ndikukonde iwe. Sukuyenera kuchita china chiri chonse ai. Siukufunikira kukhala m'zimayi wa chikhulupiro cha chikulu zedi. Chimene ukufunikira kuchita ndi kumayenda kumazungulira ndi kumandikonda ine ndi kundilora Ine kumakukonda iweyo. Ndipo nthawi yonsetu. Tangondilora ndikukonde iwe."

Ndiye, ine ndimapita kumakazungulira ndikumadzimangirira ine mwini mu chikhulupiro changa choyeretsetsa ndi kumaimba, kupanga nyimbo za kwa Mulungu ndi kukhala ndi nthawi yokoma. Kenako mwadzidzidzi ndinamumva mwamuna wanga ku garaja kuja. Koma anali atatuluka kupita ku ntchito pafupifupi mphindi makumi anayi ndi mphambu zisanu (45)! Iye anatsegula chitseko ndipo anati, "Ine sindinathe kukwanitsa kuitulutsa mugiya yoyamba ya galimoto ija. Tikuyenera kuipititsa kokhonzetsa tsopano."

Ine ndinangotseka chitseko ndi kuyamba kuseka. Si chinthu chimene ine ndinangochiganizira chabe kuchichita. Izi zinangochitika basi. Izi zinangotuluka mu mzimu mwanga, ndipo Mulungu anandisonyeza ine kuti ndi chifukwa chakuti ine ndinamulora Iye kuti andikonde m'mawa wonse wa tsiku limemelo ndiye ndinatheka kuseka. Kumulola Mulungu kukukondani inu kumatsegula zipata za chikhulupiro kutuluka kuchoka mwa inu.

Ine ndinangoyamba kuseka, ndipo ichi chinali chikhulupiriro.

Abrahamu anaseka kuseka kwa chikhulupiriro. Pamene Mulungu anabwera kwa iye ndikumuuza kuti adzakhala ndi mwana wa mwamuna, Abrahamu anabwerera m'mbuyo ndi kuseka, nanena, "Ulemerero! Ine ndakhulupirira ichi." Tsopano Sara anaseka kuseka kwa chikayiko ndi kusakhulupirira, ndipo Mulungu anamuongolera iye, koma sanaduphire pa Abrahamu. Iye sanamudzuzule Abrahamu chifukwa choseka chifukwa pali kuseka kwa chikhulupiriro.

Pamene m'dyerekezi wafika kudzakuzunzani inu ndipo akuyesera kuchita china chake chopusa ndi chosayenera, ndipo inu mukumudziwa Mulungu wanu bwino-bwino kotero kuti sizikuopysezani inu zimenezi, inu mudzingoseka muchikhulupiriro. Inu mukudziwa kuti Mulungu amakukondani inu, ndipo Iye wakuphimbisani ku ichi.

Ndiye ine ndinali kuseka za injini yathu, Mulungu anayankhula mu mtima wangabe, mu mau ang'ono, koma anali amphamvu kwambiri. Ananena kwa ine katatu konse, "Ngati iwe udzikhala chonchi ndi Ineyo, mayi Joyce, Ine sindidzakukhumudwitsa iwe." Ichi chinangokhala ngati chikuchokera m'mwamba mwa nyumba yanga. "Ine sindidzakukhumudwitsa iwe. Ine sindidzakukhumudwitsa iwe."

Inu ngati mutsamira pa Mulungu ndikumulola Mulungu akukondeni inu ndi inu kumukonda Iye, mukhoza kuiwaliratu za ntchito yonse yomayesera kuchita mu chikhulupiriro. Tangomulolani Mulungu akukondeni inu, ndipo inu mumukonde Iye, ndipo Iye adzachikwaniritsa chimenechi. Chikondi cha Mulungu chidzamuka mwa inu ndipo chidzataya mantha onse.

Mulungu amakukondani *inu!*

6



CHIKONDI CHIMAFIKIRA KONSE

“Ndipo lamulo ili (mlandu,pempho,samani) tiri nalo lochokera kwa Iye, kuti amene akonda Mulungu, akondenso m’bale wake (okhulupirira).

1 Yohane 4 ndime 21

Inu ndi mwana wa mtengo wapatali wa Mulungu. Anakuuzani izi pa Deutoronomo 7 ndime 6. Ngati muyamba kuchita munjira ya choncho, zidzayamba kusitha dzikoli. Mudzakalowa mu sitolo kokagula ndi kusekera kwakukulu pa khope yanu ndi kuyendetsa chinjinga chogulira katundu mu sitolo chija ndi kunena kuti, “Chiri chonse titachigunde ndi chodalitsika. Alleluya! Eni ake ndi odalitsika kulandira ine mu sitolo muno leroli. Ulemerero!” Ndiye mudzikangoyenda mukuimba muluzu mkati mwa sitolomo m’menemo, mukuimba, kukhala wa mtengo wapatali kuli konse komwe mukulowera.

Pamene tayamba kuzindikira kuti ndife a mtengo wapatali bwanji ndikuyambanso kumachita ngati kuti Mulungu amatikonda ife, tikhoza kulikopa dzikoli kwa Yesu. Chikondi chidzidza ngofalikira pali ponse ngati moto wa mu nkhalango. Koma sizingathandize chiri chonse kumayenda ndi kumazungulira ndi kumanena, kuti

ndine Kristu, ndikumamu ng'ung'udzira wina aliyense. Iwe umati ndine Kristu - ndine Kristu koma pamene mwadzidzi galimoto yadulira kutsogolo kwako pa msewu, iwe mokuwa umati, “Choka iwe wachabechabe pita uko. Kodi sukudziwa kuti ndikupita ku Tchalitchi ine? Ndichedwa ku msonkhanotu, opusa iwe.”

Izi ndi zina mwa zimene timachita nthawi zina. Kodi muli okonzeka kukhala nacho chogonjetso? Tangowakhani inu mu uzimu, ndikuchiwakha chigonjetsocho ndi kunena kuti, “M'dyerekezi, wandizunguza ndi chitsogozo chabodza ndi mantha nthawi yayitali tsopano. Ine ndine wa mtengo wapatali, ndipo ndikhala ndi chigonjetso tsopano mu dzina la Yesu chifukwa chakuti Mulungu amandikonda ine, m'dyerekezi, palibe chiri chonse chimene iwe ungachite konse, ai.

Chikondi cha Mulungu mkati mwa inu chidzakumasulani inu ku mantha, ndipo inu simudzakhalanso owopa kukafikira anthu ena ndi chikondi. Mulungu akufuna inu mukakhulupirire chimene Iye akunena ndipo Iye adzachita zinthu zazikulu zedi kudzera mwa inu chifukwa chakuti Yesu anapita kwa Atate ake. Kodi mukukhulupiriradi kuti Mulungu angathe kukugwiritsani inu ntchito? Mulungu adzakupatsani chimene inu muli kuchikhulupirira kuchokera kwa Iye. Inu musaope kukachichita uko.

Ine sindingathenso kukuuzani inu kuti ndi kangati kamene ine ndakhala nditaima pa mphepete pa chikhulupiriro, pamene ndiri pa mphepete peni-peni nditatsala pang'ono kuchita china chake choopsya, ndipo Mulungu anati, “Tabwera kuno, mai Joyce, tabwera kuno. Ine ndidzachita zinthu zazikulu kudzera mwa iwe. Tabwera kuno.” Ndipotu ine ndimangodupha mkatikati mwake momwemo, ndipo Mulungu sana ndikumudwitsepo ine ngakhale

kamodzi.

Mukudziwa chifukwa chiani ine sindimadandaula kukachichita chithu ndi kukalephera? Chifukwa ndikudziwa kuti Mulungu amandikonda ine. Iye amandikonda ine, ndipo Iye amadziwa kuti ine ndimamukonda, ndiponso kudzera mu chisomo chake ndinapereka moyo wanga kwa Iye. Inu ngati munachita chimenecho, ndipo mumamukonda Mulungu, ndiponso Iye amakukondani inu, ndiye kuti palibe china chiri chonse cha chilengedwe chimene chingakhale vuto kwa inu chimene simungathe kuchigonjetsa.

“Adzatisiyanitsa ndani ndi chikondi cha Mulungu? Nsautso kodi, kapena kupsyinjika mtima, kapena kuzunza, kapena njala, kapena usiwa, kapena zoopsya kapena lupanga kodi?”

Monganso kwalembewa, Chifukwa cha inu tirikuphedwa dzuwa lonse; tinayesedwa monga khosa zakupha.

Koma m'zonsezi, ife tilakatu, mwa Iye amene anatikonda.

Pakuti ndakopeka mtima kuti ngakhale imfa, ngakhale moyo, ngakhale zinthu ziripo, ngakhale zinthu ziri nkudza, ngakhale zimphamvu.

Ngakhale utali, ngakhale kuya, ngakhale cholengedwa china chiri chonse, sichingakhoze kutisiyanitsa ife ndi chikondi cha Mulungu mwa Kristu Yesu Ambuye wathu.”

Aroma 8 ndime ya 35 mpaka 39

Inu mungathe osamvetsetsa kuti kodi Mulungu akufuna inu mukhale omasulidwa mwa mtundu wanji. Mulungu amamva ululu inu mukakhala osasangalala. Nthawi zina inu mumadzuka

ndikukhala zinthu zosayenda bwino tsiku lonse. Kodi mwadziwa tsiku lake limene ndikunena kuti limakhala lamtundu wanji? Inu mumamuponda mphaka, kuwakalipira ana zosadziwika, kudana ndi oyandikana nawo, maonekedwe amene uli nawo ndi a chikalambire kalambire, oipa choncho ochita kuonekera pa khope pako. “Chimene ndimachita ndi kumangogwira ntchito, kumangogwira ntchito, kamangogwira ntchito, ndipo palibe amandithokoza ine.”

Ine ndikudziwa umo inu mumachitira chifukwa inenso ndinachitaponso, zimenezo. Pamene ana afika kunyumba, umaganizira kuti, “Chifukwa chiani iwowa amakhala nthawi yochepa kusukulu kwawoko m’ malo mokhalako nthawi yaikulu?”

Kodi mukudziwa kuti zimenezo zimamumvetsa Mulungu ululu? Ine sindikufuna kuti inu mukhumudwe ai. Ine ndingoyesetsa kufuna kuti inuyo mukazindikire kuti ngati mungakhulupirire kuti Mulungu amakukondani inu, muyamba kumachita china chake ndi chikondi chimenechi, ndipo chikondi chimenecho chidzikadzala mwa inu pang’ono pang’ono ndi kuyamba kutsanukira mosefukira kugwera wina aliyense. Inu mudzakhala omasuka kukhala okondeka wa wina aliyense, mukuyendereredwa ndi zipatso za chifundo.

Inu mukawakha choonadi chakuti Mulungu amakukondani inu, machiritso anu adzabwera ndithu, kuchita bwino kwanu kudzabweranso ndipo zosowa zanu zidzakwaniritsidwanso. Chifukwa kodi? *Inu mudzangokhala chete motakasuka.*

Chifukwa chachikulu chimene chimachititsa kuti Mulungu asamathe kutipatsa ife zinthu zambiri zimene Iyeyo amafuna kutipatsa ife ndi chifukwa chakuti ife timatanganidwa zedi kuti tizepeze zimenezozo ndiye sangathe kukumanizana nafe pena

pali ponse kuti aziike zimenezo pa ifeyo. Mulungu akufuna kuti ife tikapumule pa Iye ndikumangomukonda Iye. Iye akufuna inu mumulole Iye kukukondani inu ndi kungolandira basi.

M'dyerekezi sangathe kuimitsa kuyenderera kwake ngati inu muli wachikondi chifukwa ngati muli wachikondi, mudzakhala wopatsanso. Simungathe kukonda ndi kusapereka.

Ndime yomaliza ya mau A m'Bukhu lopatulika pa Deutoronomo 7 ndime 6 AMP akuti. "...*Yehova Mulungu anakusankhani inu mukhale inu mtundu wa pa okha.*" Mulungu wakuitanani inu. Pakali panopo ntchito yanu yaikulu ikhoza kukhala mnyumba mwanu ndi banja lanu. Inu ngati mukufunadi kuti Mulungu akugwiritseni ntchito, mukhoza kugwiritsidwa ntchito ndi Mulungu. Koma mukuyenera kukhazikitsa maziko awa pamene. *Mukuyenera kudziwa kuti Mulungu amakukondani.*

Musataye pachabe mphamvu yanu yonse ya uzimu pa inu mwini wake ndiponso kudzipezera zosowekera zanu. Mumuuze Mulungu chimene inu mukuchifuna basi ndi mwansanga msanga tsopano kumanga chikhulupiriro chanu kuti mukapeze zosowa za anthu ena. Yesu amapemphera ndi kusaka khope ya Atate Wake kuti akathe kumangika mokula ndipo kupita kukapeza zosowa za anthu ena onse amene amapita ku misonkhano Yake ya chikhulupiriro.

Ndipo Iye amakalalikira Mau kwa iwo, kukawasanjika manja pa iwo, ndipo iwo amalandira chozizwa. Iye samakhala pa tsindwi pena pake nthawi zonse kuyesera kukhulupirira Mulungu pa zinthu zimene Iye anali kuzifuna, ai. Mukufunika kumuuza Mulungu zimene inu mukufuna, koma ndizofunika kuti zingokhala za tchutchutchu basi. Chokhumba chachikuru cha moyo wanu, ngakhale kuti, chisakakhale kukwaniritsa zosowa za anthu ena.

Kuchita bwino kweni kweni, tikati tikuonetsetse, ndi kuthekera kugwiritsa ntchito kuthekera kwa Mulungu kutha kukapeza zosowekera zonse zimene zimadza kwa inu.

Chikondi cha Mulungu chimapereka kuthekera koika zosowekera za ena poyamba. Kodi mukuganizira kuti Mulungu amakukondani inu kokwana kothekera kukupangitsani inu kutheka kukawafikira ndi kukawakokonda iwo onse amene palibe chimene chingamukondweretse wina kuwakonda iwowo konse - amewa ndi aja omangoipidwa, komanso osayamika.

Sikusowekera chinthu china chake kuti mukamukonde wina wake amene iyeyonso amakukondani. Palibenso njira yapadera kuti mukatero. Aliyense wachichimwire akhoza kuchichita chimenechi. Komano pamene muwakonda iwo amene sangakondeke, inu mumabooleza ndipo mumangopitiriza kumangowakonda kondabe, ndiponso kumangopitiriza kumawakondabe, ndiponsotu *mumangopitiriza kumawakondabe*. Tsopano chikondi cha Mulungu chidzawasitha iwo.

Zikhoza kutheka kutha chaka chathuthu. Zingatenge zaka zisanu. Zingatenge zaka makumi awiri ndi mphambu zisanu, koma ndizoyenera kutero ndithu. *Kodi Yesu anakuyembekezerani inu nthawi yayitali bwanji?*

Mulungu amakukondani inu, ndipo amakondanso anthu onse amene akuzungulirani inuyo. Opulumuka kaya ochimwa, Iye amawakonda iwo, ndipo Iye akufuna kukugwiritsani inu ntchito ngati chodutsamo kukawatsanurira iwo chikondi Chake.

Musachite mantha kukachichita chimenecho. Chikondi cha Mulungu chiri nkukumasulani inu kuchoka kumantha ndi chilango, ndipo Iye wakupatsani inu kuthekera kuti mukawakonde.

Khalani okonzeka kuti mukathe kuchimwaza chikondi cha Mulungu mozungulira. Mungoyamba kukhala bwenzi la anthu. Kachipangeni chizolowezi chomakhala pa ubwenzi ndipo kukhala m'dalitso kwa anthu a mu thupi la Kristu.

Aitaneni anthu ku khumaliro ndi kumapanga anthu kuti azibwera ndiponso kudzakuchezerani inu. Kapatsaneni moni wa pa dzanja ndi anthu, kawasekererani. Mulungu ali ndi china chake chakuti inuyo mukachite. Iye akufuna kukugwiritsirani inu mu njira imene Iye sangathe kugwiritsiranso wina aliyense pa dziko lino lapansi.

Pali anthu amene ndi inu nokha amene inu mungathe kuwatumikira. Palibensi wina amene angathe kukamufikira munthu ameneyo koma *inuyo*. Kamufunsi Mulungu kuti akakusonyezeni inu njira zokafikira kumeneko ndi chikondi Chake, ndipo Iye adzakuphunzitsani inu.

Mulungu amakukondani *inu!*

7



CHIDZAKUSITHANI

“Umo muli chikondi, sikuti ife tinakonda Mulungu, koma kuti Iye anatikonda ife, ndipo anatuma mwana wahe akhale chiombolo chifukwa cha machimo anthu.”

1 Yohane 4 ndime 10

Mulungu amatikonda ife, sindikukhulupirira kuti ambiri mwa ife timatha kumvetsetsa chimenechi kwenikweni chikondi cha Mulungu m'mene amatikondera ife. Mulungu anandisonyezera ine, kudzera muzowerenga werenga zimene ndinachita za zimenezi, kuti tinakadziwadi ndithu mkati mwa mizimu yathu kuti Mulungu amatikonda ife bwanji, tinakatha kudziutsa tokha ndi kukhala osiyanilanatu ndi m'mene timakhalira nthawi zambiri.

Lingalirani pa chikondi cha Mulungu. Ichi ndi chimene chitakusitheni inu. Ngati inu pali chinthu china chake chimene simumakondwera nacho pa inuyo mwini wanu, “kudziwa kuti mumadziwa” kuti Mulungu amakukondani inu zitha kupangitsa kusitha izo.

Kodi inu mumamva bwanji mukadziwa kuti wina wake amakukondani inu? Zimakupangitsani inu kumva bwino, moyenera? Mumanva kunyansa ngati? Mulungu anandiuza

kuti ena mwa anthu amene awerenge bukuli amadzida iwo okha. Inu mumadana ndi zinthu zimene inu muli kuchita, ndipo simunavomerezebe kuti ndinu watsopano - mumangolimbana limbanabe ndi umuthu wanu wakalekaleyo.

Pamene inu muyenda yenda ndi kumazungulira musakumva bwino mwa inu nokha nthawi zonse, osakondwera ndi inu mwini, kumangodzida inu nokha, osazindikira kuti ndinu a mtengo wapatali apaderadera mwa mtundu wanji, inu simudzatha kuchita zinthu zoti ndinu wa mtengo wapatali wapaderadera. Baibulo likuti, “*Pakuti monga asinkha m’kati mwache ali wotere*” (Miyambo 23 ndime 7 AMP). Ndi chifukwa chakuti inu simunawakhe mwa ndii kwenikweni choonadi *chakuti Mulungu amakukondani inu*. Ndi chinthu cha mphamvu kwambiri zedi kudziwa kuti Mulungu amakukondani *inu* kwambiri bwanji.

Mulungu akufuna kuti inu mutengane naye Iye mu tsiku liri lonse. Ichi ndi chimene chitakusitheni inu. Ngati inu simungamuiike Mulungu poyamba, mukumuiika Iye pamalo pamene Iye sangathe kukuchitirani inu chimene Iye amafuna kutero. Ndi nthawi ya paderadera yomakhala naye Mulungu, kumangomukonda Iye ndi kumulola Iye akukondeni inu, zimenezi zidzakupangitsani inu kukula mu uzimu ndiponso kukhala a mphamvu mu mzimu wanu wa umunthu.

Gawo lalikulu la anthu ndi la ulesi iwo sangafune kuti achite zimenezo. Iwo zingakondweretsekobe wina wake atamawachitira zimenezizo. *Inu musapeze pothawira, ai*. Aliyense amene akuwerenga izi ndipo sakuyanjana ndi Mulungu ndipo akutsimikiziridwa chifukwa cha zimene ndikulembazi iye m’dyerekezi adzakhala ukumutsata ngakhale pambuyo pa kutsimikizika uku ndipo akuti, “Komatu uli ndi zina zambiri

zopanga.”

Ine ndikudziwa m'mene zimachitikira - m'dyierekezi amakupatsani inu pothawira apa ndi apo. Tadziperekani kwathuthu kwa Mulungu, ndipo mulilire kwa Iye. *Mau a Mulungu ndi kuyanjana naye kudzakusinthani inu.* Mulungu wakupangani inu kuti mukathe. Paulo akuti pa Afilipi 4 ndime 13, “*Ndikhoza zonse mwa Iye wondipatsa mphamvuyo.*” Tikhoza kungotinsu, palibe china chiri chonse mu chilengedwe chimene inu simungathe kuchichita kudzera mu mphamvu ya Yesu Kristu.

M'mene Mulungu angakusonyezereni inu vuto mwansanga, mukuyenera kumuka ndithu ndi mphamvu ndi chigonjetso ndipo ndikuligwetsera pansu limenelo. Inu mukani ndithu ndi kulandira chikondi cha Mulungu kwa inu ndipo kumukana uyo woipa, m'dyierekezi wonama kukuuzani inu kuti ndinu obvunda mwa mtundu wanji ndi kusakhala bwino komwe muli nako, inu mudzayamba kuchita zinthu mogonjetseratu.

Inu panopo mwina simukuchita bwino ai, koma mutha kuchita mosiyana ngati inu mukhulupirira kuti ndinu wolengedwa watsopano mkati mwanumo. Inu simudzatha kusiya kapena kuchita mosiyana ngakhale ndi kamodzi komwe mpakana pamene inu muyamba kumuka ndithu ndi kunena kuti, “Mulungu akwezeke, ndine wamtengo wapatali wapaderadera. Ine ndine woyera. Mulungu anandisankha. Iye wandiyeretsa ndi mwazi wa Mwana wa nkhusa. Ine ndidzichita choncho. Ndipo palibe chifukwa, m'dyierekezi, kuti ndalakuwitsa zinthu zingati. Mulungu ndi wamkulu ndithu kuti angathe kundinyamutsa ndi kundipanga ine kuti ndipitirirebe. *Iye amatsuka zonse zimene ine ndasokoneza!*”

Kodi ndi bvuto lanji limene lingakugonjetseni inu ngati inu

“mukudziwa kuti mukudziwa” kuti Mulungu amakukondani? Palibe amtundu ulionse. Inu mudzagonjetsa mu onse amenewowo.

Kodi inu mukufuna kukhala ogonjetsa? Yankhani izi ndiye - kodi mukufuna kukhala ndi china chake kuti mugonjetse? Ndi njira imeneyo yokha imene mungakule. Ngati simukhala ndi mabvuto ndipo simukhala ndi china chiri chonse choti muchigonjetsa, kodi inu mudzadulira potani ndi manu anu a chikhulupiriro?

Ka agwiritsemi mabvuto amene amabwera kwa inu ngati mwayi wakuti mukule. Kafufuzeni chimene Mulungu angachite chifukwa chakuti Iye amakukondani inu! Inu ngati mutsamira pa Mulungu ndi kumulola Mulungu kuti akukondeni inu ndipo inu ndi kumukonda Iye, mukhoza kuiwalira zonse zomayesera kuchita zinthu muchikhulupiriro ndipo mudzalowa mu mpumulo.

Ngati inu mudzalora kuti Mulungu akukondeni inu ndipo inu ndikumukonda Iye, ndiye mudzidza ngoyendayenda mukuzungulira ngati munthu woledzera nthawi zonse-oledzera mu uzimu. Apa ndi pamene zochitika mozungulira moyo wanu sizidzatha kukupezani inu chifukwa chakuti inu muli ku ngomayendayenda mozungulira kuchita zinthu mu chikondi cha Mulungu.

Pamene ine ndinabatizidwa ndi Mzimu Woyera, milungu itatu yoyamba zinali ngati wachiledzere ndi chikondi cha Mulungu. Anthu ankangofunsa kwa ine, “Chabvuta ndi chiani ndi inu kodi? Ndinu wa mtundu wina tsopano. Ine sindikukhulupirira izi, mai Joyce. Kodi chakuchitikirani inu ndi chiani?” Anthu omwewa anandipezanso patadutsa milungu itatu ija ndipo anati, “Kodi chachitika m’ moyo mwanu ndi chiani?”

Sindinafunikire kunena ngakhale mau amodzi kuti

ndikawatsimikizire iwo kuti ndasintha. Iwo amatha kuziona zimenezo. Inu ngati muchita zinthu mu chikondi cha Mulungu, inu mudzakhala mukumwetulira nthawi zonse. Mudzakhala okongola. Mudzakhala ndi kulimbika kochita chita ndi mphamvunso. Inu mudzatha kutumikira anthu chifukwa inu mudzakhala mutapeza nyonga zochoka kwa Mzimu Woyera nthawi zonse kotero kuti chosowa chanu chiri chonse chomwe mudzakhala nacho chidzakwaniritsidwa.

Tadziuzani nokha mwini wanu, “*Mulungu amandikonda ine. Alleluya, Mulungu amandikonda ine.* Ndine wamtengo wapatali wa paderadera. *Mulungu amandikonda ine!*” Tsopano pitani m’chitsogolo - mudzipatse ndime yaikulu ya chikhulupiriro ndipo mukakhulupirire chimenecho.

Mulungu amakukondani kwenikwenidi *inu!*

MUKHALE M'MOYO WATSOPANO



Ngati inu simunamuitane Yesu kukhala Mbuye ndi Mpulumutsi wanu, ine ndikukuitanani inu kuti mutero tsopano. Inu mungathe kupemphera pemphero iri, ndipo ngati inu muli kutsimikazadi, mudzakhala ndi moyo watsopano mwa Yesu.

Atate Mulungu, ine ndimakhulupirira kuti Yesu Kristu ndi Mwana Wanu, Mpulumutsiyo wa dzikoli. Ine ndikukhulupirira Iye anandifera ine pamtanda, ndipo anandisenzera machimo anga onse. Iye analowa mu gahena ndipo anaigonjetsa imfa ndiponso manda. Iye anatenga chilango chimene chinali cha ineyo. Ine ndikhulupirira kuti Yesu anauka kwa akufa ndipo tsopano wakhala kudzaja Lanu la manja. Ine ndi kufunane Inu, Yesu. Ndikhulukireni machimo anga, bwerani mudzakhale mkati mwanga. Ndikufuna kuti ndibadwense kwatsopano.

Tsopano khulupirirani kuti Yesu akukhala mu mtima mwanu. Inu mwakhulukiridwa ndi kuyeretsedwa, ndipo pamene Yesu adzabwera, inu mudzapita kumwamba.

Pezani mpingo wabwino umene uli kuphunzitsa mau a Mulungu ndipo mukule mwa Yesu. Palibe china chiri chonse chimene chingasinthike m'moyo mwanu popanda kudziwa mau a Mulungu. Yohane 8 ndime ya 31 ndi 32 (AMP) ikuti, "... Ngati mukhala inu m'mau anga, muli akuphuzila anga ndithu. Ndipo mudzazindikira choonadi, ndipo choonadi chidzakumasulani."

Ndikukulimbikitsani kuti muwagwiritsitse Mau a Mulungu, muwadzale mkati mwa mtima mwanu, ndipo monga pa 2 Akorinto

3 ndime 18, mukamawerenga m’Mau, inu mudzasandulika kukhala ndi chithunzi-thunzi cha Yesu Kristu.

Mundilembere ndi kundidziwitsa kuti mwalandira Yesu ndi kufunsa kabukhu kaulere ka m’mene mungayambire moyo wanu watsopano mwa Khristu.

Ndine wanu wa chikondi,

Mai Joyce

PEMPHERO LA CHIPULUMUTSO

Mulungu amakukondanani ndipo akufuna kuti kukhale pa ubale wabwino. Ngati simunamulandire Yesu ngati mpulumutsi, mukhoza kumulandira tsopano. Tsekulani mtima wanu kwa Yesu ndi kupemphera pemphero ili...

“Atate ndikudziwa ndakuchimwirani, mundikhululukire. Ndisambitseni. Ndikulonjeza kukhulupilira Yesu mwana wanu. Ndikukhulupilira anandifera – ananyamula machimo anga pamene anafa pa mtanda. Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndikupereka moyo wanga kwa iye tsopano.

Zikomo atate chifukwa cha mphatso ya chikhulukiro ndi moyo wosatha. Ndithandizeni kukhala moyo wa inu mdzina la Yesu, amen.

Monga momwe mwapempera mu mtima mwanu, Mulungu wakulandirani, wakuyetsani ndikumatulani ku ndende ya imfa ya uzimu. Pezani nthawi ndikuwerenga mawu awa ndikufunsa Mulungu akulankhuleni pamene mukuyenda naye mmoyo watsopanowu.

Yohane 3:16

1 Akorinto 15:3-4

Ayefeso 1:4

Ayefeso 2:8-9

1 Yohane 1:9

1 Yohane 4:14-15

1 Yohane 5:1

1 Yohane 5:12-13

Pempherani kuti Yesu akuthandizeni kupeza mpingo wophunzitsa ndi kukhulupilira Baibulo kuti mulimbikitsidwe ndikukula muchiyanjano ndi Yesu Christu. Mulungu alinanu nthawi zonse akutsogolerani tsiku ndi tsiku ndipo akuwonetsani mmene mmene mukhalire mmoyo watsopano!

ZA OLEMBA BUKHULI



Mai JOYCE MEYER wakhala akuphunzitsa za Mau a Mulungu kuyambira chaka cha 1976 ndinso mu utumiki wamphumphu kuyambira chaka cha 1980. Iyeyu ndi munthu amene mabuku ake agulitsidwa kwa mtengo wa patali kwambiri pa mabuku oposera makumi asanu ndi mphambu zinayi, kuphatikizirapo mabuku awa; *Secrets to Exceptional Living* (Zinsinsi za Chikhalidwe cha Padera), *The Joy of Believing Prayer* (Chimwemwe cha Pemphero la Chikhulupiriro) ndi *Battlefield of the Mind* (Bwalo la nkondo la m'malingaliro), pamodzinso ndi ma alabamu a makaseti omvetsera oposera mazana awiri ndi mphambu makumi awiri ndinso a vidiyo okwanira makumu asanu ndi anayi. Mapologalamu amayi Joyce otchedwa *Life in the Word* (Moyo wa m'mawu) ndi mapologalamu apa tivii amaulutsidwa kuzungulira dziko lonse la pansu, ndipo amayi Joyce amayenda kwambiri kugawana maulaliki ake mu misonkhano yotchuka zedi ya "Life in the Word" (Moyo wa m'mawu). Mayiyu Joyce ndi abambo akunyumba kwawo a Dave ali ndi ana anayi ndipo amakhala ku St. Louis, ku Missouri.